

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

MALANGIZO NDI CHILIMBIKITSO KUCHOKERA M'BAIBULO
KUPITA KWA AMENE AKULALIKIRA UTHENGA WABWINO

MFARISI NDI WOKHOMETSA MSONKHO

(Nkhani yotsatirayi ndiyo kufotokozera kwa Fanizo limene Yesu ananena pa Luka 18:9-14).

CHIYAMBI CHAWO:

Gulu la Afarisi linali limodzi la mabungwe aakulu ndi lolemera kwambiri pakati pa mabungwe a Ayuda. Iwo amatsatira mosamalitsa ambiri mwa malamulo a Mose ndipo amatsatiranso kwambiri miyambo ndi zinthu zimene Mose ananena. Dzina lakuti Mfarisi litanthauza *Wodzipatula*. Iwo amadzipatula ku chidetsu cha chipembedzo cha Chiyuda ndipo amayima paokha ngati gulu la anthu oyeretsesa ndi osadetsedwa. Iwo amatsatira malamulowo a bungwe laolo ndipo amadzilungamitsa chifukwa chakuti amatsatira malamulo. Poyambayamba iwo anali ovomerezeka kwa Mulungu, koma kenaka Afarisi ambiri anataya chauzimu komanso cholinga cha lamulo ndipo anakhazikika pa kuyeretsedwa kwa zinthu zowonekera kunja kusiyana ndi za mu mtima. Chipembedzo chao chinali chongodziwonetsera popeza amafuna kuti anthu adziwayamikira. Chimene chinatsalira mwa iwo ndi chikhalidwe cha chipembedzo popeza ambiri mwa iwo anakhala odzikuza ndi odzilungamitsa, namawaona anthu ena mowanyoza.

Anthu okhometsa msonkho anali anthu

wamba ndi osawerengeredwa pa chipembedzo cha Chiyuda. Kawirikawiri iwo anali Ayuda koma amatumikira boma la Chiroma limene limawalamulira Ayudawo. Iwo amanyozedwa ndi Ayuda anzao chifukwa amaonedwa ngati owukira chifukwa amatolera misonkho mmalo mwa



boma lozunza la Chiroma. Nthawi zambiri iwo amachita katangale ndi chinyengo pamene amagwira ntchito yao.

FANIZO:

Mfarisi analowa mu kachisi molimba mtima. Mikanjo yake yaitali inali yambakatayambakata ndipo mwamatama anamudutsa munthu wokhometsa msonkho amene amayenda mozojolika kukalowanso mu kachisi momwemo kuti akapemphere.

Mfarisi uja anamuyang'ana Wokhometsa Msonkho uja monyogodola ndipo anachokapo posafuna kudetsedwa ndi uchimo wa Wokhometsa Msonkhoyo.

Ataimirira chapatali poteropo. Mfarisi uja anakweza manja ake m'mwamba napemphera. Mau ake ofuula anamveka mu kachisi monse pamene amapemphera. Iye anati:

"Mulungu, ndikuyamikani kuti sindili monga anthu onse ena, opambapamba, osalungama, achigololo, kapenanso monga wamsonkho uyu; ndisala chakudya kawiri sabata limodzi; ndipereka limodzi la magawo khumi la zonse ndili nazo."

Mfarisiyo anapitiriza kupemphera uku akukweza Mulungu ndiponso kulemekeza, anayamikira ntchito zake zabwino

komanso chilungamo chake. Monga mmene amachitira munthu akadzimvera chisoni, wamsonkhoyo alikuima patali sanafune kungakhale kukweza maso kumwamba chifukwa chakuti anadziona kuperewera, komatu anadziguguda pachifuwa pake ndi kupwetekedwa mtima, pemphero lake silinali lofuula kuti anthu akhoza kumva zomwe amanena. Iye anati:

"Mulungu, mundichitire chifundo, ine

(Yapitirira pa tsamba 2)

Mau a Mkonzi

3

Kusanthula Mau a Mulungu: Kudzilungamitsa

4

Nkhani yothandiza pa kusanthula Baibulo: Kudzilungamitsa

5-6

Mafunso ndi Mayankho

7

Kodi Mukudziwa?

Mau a pa Nyengo yake

8

zimene BAIBULO limaphunzitsa za...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; I Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;

Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

I Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chihero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; I Pet. 1:15-16;

Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; I Akor. 12:12-13;

Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;

I Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chihero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;

I Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

I Tim. 2:9-10; I Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;

Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

wochimwa."

PHUNZIRO:

Yesu ananena fanizo limeneli kwa ena amene anadzikhulupirira mwa iwo okha kuti ali olungama, napeputsa onse ena. Iye anati, "Ndinena ndi inu, anatsikira kunyumba kwake woyesedwa wolungama uyutu, wosati uja ai; pakuti yense wakudzikuza yekha adzachepetsedwa; koma wodzichepetsa yekha adzakulitsidwa."

Mfarisi uja anali ndi maonekedwe a chipembedzo ndipo amatsatira mfundo zambiri zimene zinali zabwino, koma mtima wake unali wodzikuza. Iye amadzilungamitsa ndipo amadziona kuti anali wauzimu kwambiri kuposa anthu ena onse. Ntchito zake zabwino ndiponse nsembe zake sizinampulumutse. Wokhometsa msonkho uja, ndi mtima wodzichepetsa, anapempha kuti Mulungu amuchitire chifundo. Iyeyutu ndi amene anakhululukidwa tchimo lake napulumutsidwa pa tsiku limenelo.

Chipulumutso chili mphatso ya Mulungu kwa iwo amene adzichepetsa okha ndi kuvomereza kuchimwa ndi kuperewera kwawo. Kukhala munthu wabwino, chipembedzo ndi kuchita ntchito zabwino izi sizilungamitsa mtima wa munthu. Mpingo walero ukufunsidwa kuti udzipatule ku uchimo wa dziko lapansi. Pamene wadzipatula chomwecho, mwana wa Mulungu aliyense apembedze ndi kukhala m'moyo wodzichepetsa mumtima mwake ndi kusalola kuti allowedwe ndi mtima wa uFarisi ndiponso wa kudzilungamitsa yekha. Chilungamo choona chenicheni sichi-chokera kwa ife koma kwa Ambuye.

—mws

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa mkalata umene umasindikizidwa m'dzina la Ambuye kwa anthu onse ku maiko onse ndi cholinga chofuna kuwakhazikitsa ndi kuwalimbikitsa mu choonadi cha Mau a Mulungu. Kalata uyu akuphunzitsa ndi kulimbikitsa zoona za Baibulo zimene zakhazikitsidwa kuyambira pa nthawi ya Khristu ndi ya atumwi.

Mau a Mulungu ndi okhawa amene ali muyeso wovomerezeka wa chikhulupiriro. Amaphunzitsa chipulumutso ndi mamasulidwe kuchokera ku uchimo kudzera mu ntchito ya maomboledwe ya mwa Yesu Khristu; komanso kudzazidwa ndi Mzimu Woyera kumene kumatsatirapo. Ndipo kumatithandiza kuti titsogolere, tiwongolere ndi kuwapatsa ena mphamvu; komanso tikhale ndi chihero choonekera pa gawo lililonse la moyo wa munthu kuphatikizapo mgwirizano ndi umodzi wa anthu a Mulungu. Utumiki wovomerezeka wa kwa Mulungu uli mu mwa anthu amene ubale wao wachikondi wazikika pa choonadi.

Akonzi: Michael & Rene Smith

KUTI MULANDIRE NAWO KALATAYI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa kalata umene timasindikiza miyezi itatu iliyonse molingana ndi chitsogozo cha Ambuye. Kuti mulandire nawo kalatayi mwaulere pa email, pitani pa intaneti ndipo mutipeza pa www.thegospeltruth.org. Muli omasuka kutitumizira maina ndi ma email a anthu amene akufuna kulandira nawo kalatayi. Mainawa muwatumize kwa mkonzi.

KUTI MUTIPEZE

Uthenga Wabwino wa Choonadi imasindikizidwa mu maiko osiyanasiyana kuti igawidwe m'maikowo. Ntchito yosindikiza kalatayi komanso maumiki ena ochitika ndi ofesi yathu pothandiza kufalitsa uthenga wabwino amathandizidwa ndi zopereka zaufulu zoperekedwa mdzina la mpingo wa Mulungu.

Mau a Mkonzi



Iye anakuuza, munthuwe, chomwe chili chokoma, ndipo Yehova afunanji nawe koma kuti uchite cholungama, ndi kukonda chifundo ndi kuyenda modzichepetsa ndi Mulungu wako? —Mika 6:8

Ifeyo tili ndi ngongole kwa Mpulumutsi wathu imene sitingathe kulipira. Ife tinali osayenera ndi osawerengedwa kulandira chisomo ndi chikondi chake, komabe iye anatikhululukira. Pali ziphunzitso zambiri zofunikira mu Baibulo koma kudzichepetsa ndicho chimodzi mwa ziphunzitso zazikuluzo. Mulungu amafuna mwana wake aliyense kuti ayende m'moyo wa kudzichepetsa ndi wachikondi. Ndi chomvetsa chisoni kuona mzimu wa kudzikuzwa ukuonekera pa anthu amene ali ndi chidziwitso cha choonadi chachikulu.

Mtolo wa katundu amene Mulungu anaika pa mtima panga ulendo uno uli pa mutu wa Kudzilungamitsa. Ngakhale kumeneko kuli ngati kuthawa kuchokera pa magawo a ziphunzitso zoonadi za umulungu zimene taphunzira mu nyengo zapita m'mbuyomu, chimenechi chili chiphunzitso chofunikira kwambiri. Tikhoza kukhala ndi chizindikiritso cha ziphunzitso ndi zoonadi zochulukira; koma ngati tili odzikuzwa mu uzimu ndi kumadalira ntchito zathu, tidzasemphana ndi madalitso enieni a Ufumu wa Kumwamba m'moyo uno ngakhale m'moyo umene ulinkudza.

Ndikumbukira bwino ndithu kuti ndili mwana ndinaona gulu la anthu ena amene anayamba kulemekeza chiyero chao. Zambiri zimene iwo amachita zinali zabwino ndi zolondola, koma anakutidwa ndi mzimu wankhanga ndi zongodzudzula zilizonse. Iwo amadzilungamitsa ndipo anakwezwa njira ndi zochitika zao ngati njira yopitira kwa Atate. Ndimakumbukira abambo anga ondibereka akundiuzwa kuti ngati pa choonadi chilichonse tichotsapo chikondi, ndiye kuti tataya zonse basi. Nkofunikira kwa ifeyo ngati ana a Mulungu kuti tidziyenda mu chikondi komanso kudzichepetsa. Palibe chimene tingachite kudzera mu mphamvu zathu pofuna kuti Mulungu atikomere mtima kapena kuti tikhale abwino pamaso pake.

Tsiku ndi tsiku ndimadalira chifundo ndi thandizo lochokera kwa Mulungu pofuna kuti tikwanitse kukhala m'moyo wa chiyero. Chidzikhala chokhumba chathu kuti tidzibereka chipatso chabwino ndiponso kuti tidzikhala achangu pochita ntchito zabwino. Ntchito zimenezo si malipiro a chipulumutso chathu koma ndi chitsimikizo cha Khristu mkati mwathu.

Mu kulankhula kwathu, kulalikirira kwathu, m'moyo wathu komanso ngakhale mu mzimu wathu umene, tizikhala mwakuti Khristu azilemekezeka. Ena mwa anthu ovuta kwambiri kukhala nawo pakati pathu ndi iwo amene amadalira ntchito zao ndiponso kuganiza kwao koma amakhala kuti ndi amwano komanso odzikuzwa mu uzimu. Pali anthu ena amene sangapepese ngakhale atakhala kuti achita chinachake cholakwa ku uzimu. Kudzilungamitsa ndi chinthu chonyansa kwambiri. Chimenechi chimaneonekera pamene anthu achita changu choposera muyeso kapenanso aonetsa moyo wolekerera.

Tilole kuti Khristu akwezeke m'miyoyo yathu komanso mu thupi la Khristu. Tilibe chipulumutso kapena chisomo kuti tipereke ku mtundu wa anthu mwa mphamvu zathu, koma tikhoza kuloza kwa iye amene anafa m'malo mwathu. Tilole kuti dziko liwone Khristu ndipo iye ndi amene ayenera kuonekera, popeze iye ndiye woyamba ndi wotsiriza wa chikhulupiro chathu.

Michael W. Smith

July 2015

Zambiri Zili pa
INTANETI

Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.us

kuti mudzilandira

makalata athu kapenanso

kuti muone makalata

akale.



KUSANTHULA MAU A MULUNGU

MUTU: KUDZILUNGAMITSA

Zijazo munayenera kuzichita...

(Mateyu 23:23-24; Luka 11:42)

Kangapo konse Yesu analankhula ndi Afarisi amene amakonda kudzilungamitsa. Khristu sananyoze moyo wao wosamala malamulo kapena kuonetsetsa kuti malamulowo akutsatidwa; koma anawadzuzula chifukwa sanalabadire zinthu zofunikira monga - chilungamo, chifundo, chikhulupiriro ndi chikondi pa Mulungu.

"Zijazo munayenera kuzichita, osasiya izi zomwe."

Monganso mmene amachitira anthu amene amadzilungamitsa masiku ano, Afarisi amasalitsa kwambiri miyambo ina koma kunjani nkumaonetsa mzimu wachikunja ndi wopanda chikondi.

Anthu ena amadzilungamitsa pa chikhulupiriro chawo mpaka kufika pokana mankhwala a ku chipatala. Ena chilungamo chawo chili mu kuvala modzilemekeza. Ena amapeza chilungamo chawo mu kupereka. Ena mwa anthu amenewa amasowa chikondi ndi kudzichepetsa zimene zimapezeka mwa Khristu.

Pitirizani kukhala omvera ndi osamala pa zinthu zakunja koma musayiwale kuchita zinthu zofunikira zauzimu.

Kuwerenga Mau a Mulungu: Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiriro, ndipo ichi chosachokera kwa inu: chili mphatso ya Mulungu; chosachokera kuntchito, kuti asadzitamandire munthu aliyense. —Aefeso 2:8-9

Kunena Mwachidule: Kudzilungamitsa ndi kosiyana ku choona cha uthenga wabwino ndipo kumabweretsa imfa ya uzimu. Sitichita kugula chipulumutso koma ndi mphatso ya Mulungu. Nhawi zonse, ulemerero wonse uyenera kuperekedwa kwa Atate ndipo usapite kwa iwe mwini kapena kwa chilichonse chimene anthu achikhazikitsa.

I. Zizindikiro za anthu Odzilungamitsa okha

- Luka 10:29 Amadzilungamitsa pamaso pa anthu.
- Mateyu 23:27-28 Amaoneka olungama kunjani koma mkati ndi odzaza ndi chidetso.
- Mateyu 6:1-2 Amakonda kuti aonedwe ndi anthu.
- Aroma 10:1-3 Amakhazikitsa zilungamo zaozao.
- Mateyu 7:3-5 Amafulumira kuloza zofooka za anthu ena.
- Luka 7:39 Amaweruzana anthu ena kuti ndi olakwa.
- Yesaya 65:5, Luka 18:9 Amadzikweza okha ndipo amachepetsa anthu ena.
- Miyambo 20:6 Amalalikira za ubwino wao wokha.
- Miyambo 30:12 Amadziona okha kuti iwo ndi oyera.

II. Chilungamo chathu chathu

- Luka 11:42-44 Ndi chakunja.
- Yesaya 64:6 Ndi chokhala ngati chovala chodetsedwa.
- Yesaya 57:12 Ndi chosapindulitsa.
- Luka 16:15 Ndi chonyansa pamaso pa Mulungu.

E. Chibvumbulutso 3:16-17

Chimatipangisa kuti tisaone.

F. Mateyu 5:20 Chidzatilepheretsa kukalowa kumwamba.

III. Chilungamo chenicheni ndiponso kuyesedwa wosachimwa kwenikweni

- Aefeso 2:8-9 Sichichokera kwa ife eni koma ndi mwa chisomo.
- Agalatiya 2:16 Si mwa lamulo koma mwa chikhulupiriro.
- Tito 3:5 Si mwa ntchito koma mwa chifundo.

IV. Chithunzi cha Ulemerero

- Yesaya 42:8 Mulungu samagawana ulemerero wake ndi wina aliyense.
- Daniele 4:28-31 Chitsanzo cha Nebukadinezara.
- 2 Akorinto 10:17-18 Ulemerero mwa Ambuye.
- Mateyu 5:16 Ntchito zopereka ulemerero kwa Atate.

Kumaliza:

Njira zonse za munthu zilungama pamaso pake; koma Yehova ayesa mitima. Kuchita chilungamo ndi chiweruzo kupambana ndi nsembe kumkonda Yehova. Maso akunyada, ndi mtima wodzikuzana, ndi nyali ya oipa, zili tchimo. —Miyambo 21:2-4

KUDZILUNGAMITSA

Nkhani yothandiza pa kusanthula Baibulo

CHIPULUMUTSO CHILI MPHATSO YOCHOKERA KWA MULUNGU

Chipulumutso ndi chinthu chochitika mwaulegere chochokera kumwamba chimene Mulungu amapereka kwa iwo amene adzichepetsa ndi kulapadi machimo ao. Chipulumutso sichilandiridwa kudzera mu mphamvu za munthu, kapena mu nkhangono kapenanso mu kuthekera kwake, komatu ndi ntchito yodabwitsa ya Mulungu. Malemba amachenjeza kuti icho ndi "chosachokera kuntchito, kuti asadzitamandire munthu aliyense" (Aefeso 2:9). Kudzilungamitsa ndiko kukhulupirira kwakukulu mwa ubwino wa iwe mwini, zimene umaganiza ndi kuchita kwina ndi kumakhulupirira kuti za anthu ena ndi zolakwika. Ndipotu pali ambiri amene akhoza kukhala kuti anachita tchimo limeneli la kudzilungamitsa. Mwana wokhulupirira wa Mulungu amene akudzilungamitsa ndiye amene adalira mu ubwino wake ndi ntchito zake pofuna kuti ayasedwe wosalakwa pamaso pa Mulungu. Yesu anatenga gawo lalikulu la nthawi ya utumiki wake panso pofuna kuwadzudzula awo amene anali odzikuzi mu uzimu ndi amadzilungamitsa okha. Khristuyo anachenjeza kuti "penyani kuti mupewe chotupitsa mkate cha Afarisi," chotupitsa chimenecho ndicho chiphamaso, kudzilungamitsa komanso kuganiza kolakwika kodalira kuthekera ndi udindo umene munthu ali nawo.

CHIYERO CHILI CHOTHEKA POKHAPOKHA KUDZERA MWA KHRISTU NDI MZIMU

Onse anachimwa ndipo anaperewera pa ulemerero wa Mulungu ndipo akufunika Mpulumutsi. Anthu akhoza kukhala m'moyo woyera kudzera mwa Khristu yekha. Chifukwa cha ichi, ulemerero ndi ulemu wonse uyenera kupita kwa Atate ndipo palibepo mpata wakuti munthu adzikweze kapena kudzitamandira ku uzimu. Mtumwi Paulo anati, "Ndinapachikidwa ndi Khristu; koma ndili ndi moyo; wosatinso ine ai, koma Khristu ali ndi moyo mwa ine..." (Agalatiya 2:20). Chisomo chonse ndi kuthekera konse kuti tikhale m'moyo wovomerezeka pamaso pa Mulungu umachokera kudzera mu ntchito ya Khristu ndi mu chidzalo cha Mzimu Woyera. Koyang'ana ndi kodalira kwathu kudzikhala pa mphamvu ya Mulungu, osati pa kuthekera kotepatepa kwa munthu.

ZIZINDIKIRO ZA MTIMA WA KUDZILUNGAMITSA

Iwo amene amadzilungamitsa amadziwika ndi machitidwe angapo amene amafotokozedwa m'Mau a Mulungu. Zimafunika kuti munthu woyera wa Mulungu achenjere ndi tchimo limeneli komanso kulizindikira pamene likufuna kutumphuka m'moyo wake. Anthu amene amadzilungamitsa okha amakonda kudziyenera (Luka 10:29) pamene miyoyo yao sifikapo pa zimene Baibulo limaphunzitsa. Monga mmene Afarisi anaonetsera chitsanzo, nthawi zambiri anthu otere amangotsatira kwathunthu malamulo ochepa koma amene ali

owonekera kuti potero iwo aoneke ngati ndi olungama. Yesu anati iwo amaoneka okongola kunjika koma mkati mwao ndi modzaza ndi chiphamaso komanso chinyengo (Mateyu 23:27-28). Iwo amakonda kuti adzikwezedwa ndiponso kuoneka ngati okonda zopemphera (Mateyu 6:1-2).

KUKHAZIKITSA CHILUNGAMO CHA IWE MWINI

Paulo analankhula za iwo amene amayendayenda "pofuna kukhazikitsa chilungamo cha iwo okha, iwo sanagonja ku chilungamo cha Mulungu" (Aroma 10:3). Anthu odzilungamitsa okha amalola kuti




maganizo ao ndi zofuna zao zikhale pamwamba pa Mau a Mulungu. Iwo amafulumira kulengeza za ubwino wao wokha (Miyambo 20:6) ndipo amadziona okha kuti ndi oyera (Miyambo 30:12). Nthawi yonseyi mitima yao imakhala yodetsedwa ndi yodzikuzi. Iwo amanena ndi kudziona kuti ndi oyera (Yesaya 65:5) koma ntchito zao zimakhala zosavomerezeka ndi Mulungu.

Anthu odzilungamitsa okha amakonda kuweruza ndi amathamangira kunena anthu ena kuti ndi olakwa (Luka 6:41). "Ndipo upenya bwanji kachitsotso kali m'diso la mbale wako, koma mtanda uli m'diso la iwe mwini suaganizira?" (Mateyu 7:3).

CHILUNGAMO CHA MUNTHU CHIMAKHALA CHAKUNJA KWAKE

Chilungamo cha Mulungu mkati mwa munthu chimamutsogolera munthuyo ku moyo wachiyero woonekera motsogozedwa ndi mtima wa kudzichepetsa ndiponso wachikondi. Pamene chilungamo cha munthu chimakhala chakunja (Luka 11:42-44) ndi chokhala ngati chovala chodetsedwa pamaso pa Mulungu (Yesaya 64:6). Munthu payekha alibe chilungamo chakechake ndiponso alibe mphamvu

(Yapitirira pa tsamba 6)



“Pamene Mulungu
asiya kulandira ulemerero,
**ULEMEREROWO
UMACHOKA.”**

(Kuchokera pa tsamba 5)

yakusinthwa mtima wake popanda mphamvu ya Mulungu. Chilungamo chonse cha munthu chimakhala chosapindulitsa (Yesaya 57:12). Ntchito zabwino ndi zothandiza ndithu koma popanda mphamvu yakuchita mkati mwathu yochokera kwa Mulungu, sizingakhale ndi phindu lamuyaya.

ANTHU ODZILUNGAMITSA OKHA SAKALOWA KUMWAMBA

Kudzilungamitsa kumamupangitsa munthu kuti achite khungu ndipo nthawi zambiri anthu amanyengezedwa kuti ali wauzimu koma pamene zisali choncho. "Chifukwa unena kuti ine ndine wolemera, ndipo chuma ndili nacho, osasowa kanthu; ndipo sudziwa kuti ndiwe watsoka, ndi wochititsa chifundo, ndi wosauka, ndi wakhungu, ndi wausiwa" (Chibvumbulutso 3:17). Mpingo wa ku Laodikeya umadziona ngati ndi wachikwanekwane ndi wolemera mu uzimu, koma popanda chikondi chenicheni cha kwa Mulungu, mu kudzilungamitsa kwaoko, iwo anali osauka, amaliseche, ndi akhungu. Anataya mtima wodalira Mulungu nayamba kukhazikika pa miyambo yao yokonda ntchito zabwino. Kudzilungamitsa ndi uchimo ndithu ndipo zikhoza kumulepheretsa munthu kukalowa kumwamba. Yesu anati, " ngati chilungamo chanu sichichuluka choposa cha alembi ndi Afarisi, simudzalowa konse mu Ufumu wa Kumwamba" (Mateyu 5:20).

MAONEKEDWE A CHIPEMBEDZO

Afarisi anali nawo maonekedwe a chipembedzo. Iwo amapemphera, amasala zakudya, amapereka chakhumi ndi zina koma iwo amakhulupirira mwa zimene amachita bwino koma osati mu chisomo cha Mulungu chimene chimapulumutsa. "Munthu sayesedwa wolungama pa ntchito ya lamulo, koma mwa chikhulupiriro cha Yesu Khristu... pakuti palibe munthu adzayesedwa wolungama ndi ntchito za lamulo" (Agalatiya 2:16). Munthu akhoza kutsatira ziphunzitsa zampingo zambiri zokhudza Mau a Mulungu ndipo namavala modzilemekeza kwambiri. Iye akhoza kumapereka mwa umataya ndi kumapemphera kwambiri. Iye akhoza kukhala wokhulupirika pa chipembedzo cha mpingo komabe ndi kusemphana ndi kumwamba chifukwa akusowa mzimu wa

chikondi, kudzichepetsa ndi kudalira pa chilungamo cha Yesu yekha. Ngakhale zinthu zakunja ndi miyambo zili zofunikira, chiyero chenicheni chimayambira mu mtima.

Kodi Mumaika Mtima pa Chiyani?

Kudzilungamitsa kumaika mtima pa munthuwe kusiyana ndi pa Mulungu. Mulungu sadzagawana ulemerero wake ndi wina aliyense (Yesaya 42:8). Pamene Mulungu wasiya kulandira ulemerero, ulemererowo umachoka. Ulemerero sitingathe kuulongosola ponena za mmene gulu anthu ena oyera mtima okhulupirira akufuulira kapena mmene angavalire. Ulemerero ndi kudzoza kwa kumwamba kochokera kwa Mulungu mu zochitika za moyo wa tsiku ndi tsiku umene umabweretsa mtendere, chimwemwe, chikondi ndi kudzichepetsa. "Koma iye wodzitamandira adzitamandire mwa Ambuye; pakuti si iye amene adzitama yekha, koma iye amene Ambuye amtama ali wovomerezeka " (2 Akorinto 10:17-18). Pamene mwana wa Mulungu aonetsa ntchito zabwino pamoyo wake, izi zidzichitika ndi cholinga chakuti alemekeze Atate ake amene ali Kumwamba (Mateyu 5:16).

Chenjerani ndi chotupitsa buledi cha Afarisi. Kudzilungamitsa kukhoza kulowerera mwa munthu kapena gulu la anthu. "Ambuye, tithandizeni kukhala m'moyo wodzichepetsa, osadalira mu ntchito zathu za chilungamo koma mu zimene Khristu anachita kudzera mwa mwazi wa Yesu Khristu. Amen."

—mws



KODI NTCHITO ZABWINO ZILI NDI PHINDU LOTANI NGATI SIZINGATHE KUTIPULUMUTSA?

Aefeso 2:8-9 ndi lemba lofunikira kwambiri ndipo limagwiritsidwa ntchito nthawi zambiri. "Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiriro, ndipo ichi chosachokera kwa inu: chili mphatso ya Mulungu; chosachokera kuntchito, kuti asadzitamandire munthu aliyense."

Chipulumutso ndi ntchito ya kumwamba ya Mulungu yochitika mu mtima mwa munthu imene sanayenera kuyilandira kapena sanayigwirire ntchito. Chimenechi ndi choonadi chodabwitsa koma ambiri amayiwala vesi 10 imene imanena kuti, "Pakuti ife ndife chipango chake, olengedwa mwa Khristu Yesu, kuchita ntchito zabwino, zimene Mulungu anazipangiratu, kuti tikayende m'menemo."

Pali Akhristu okhulupirira ambiri amene amalengeza zakuti chisomo chopulumutsa cha Mulungu chikuchita pa moyo wao komabe palibe chimene chasintha pa ntchito zao, makhalidwe ao ndi kaganizidwe kawo. Iwo amagwiritsa ntchito chisomo kukhala chophimba anthu mmaso kapena chonamizira chabe pofuna kuchita ntchito zoipa ndi kuchita kusamvera ku Mau a Mulungu. Ifetu sitipulumutsidwa kudzera mu ntchito koma timalengedwa kuti tichite ntchito zabwino ndi kutinso tiyendemo mmenemo. "...pakuti monga inu munapereka ziwalo zanu zikhale akapolo a chonyansa ndi a kusaweruzika kuti zichite kusaweruzika, inde koteru tsopano

perekani ziwalo zanu zikhale akapolo a chilungamo kuti zichite chiyeretso" (Aroma 6:19).

Yesu ananena kuti tidzawadziwa anthu malingana ndi zipatso zao, kapenanso ntchito zao (Mateyu 7:16-17). Kawirikawiri, ntchito za anthu zimaonetsa chimene iwo ali mkati mwao. Mitima siyeretsedwa pochita ntchito monga kusala kudyu, kupemphera, kupereka, kupereka nsembe, kukhala munthu wabwino, kupita ku tchalitchi, kutumikira ndi zina zotere, koma ngati munthu apulumutsidwa mwa chisomo cha Mulungu, ntchito zabwino zidzakhala chipatso cha mtima wangwiro.

Baibulo limapereka malangizo ochuluka a mmene abale oyera mtima ayenera kukhalira ndi kuchitira monga anthu oyera a Mulungu. Iwo ayenera kudzipatula ndi kudziyanitsa ku dziko lauchimoli osati m'maganizo ndi m'matumikiridwe mokha komanso m'mavalidwe ndi m'machitidwe a



moyo wao.

Yesu anati, "Ngati wina akonda Ine, adzasunga mau anga...Wosandikonda Ine sasunga mau anga" (Yohane 14:23-24). Kumvera kumabweretsa ntchito zabwino. Ntchito zabwino sizipulumutsa munthu, komabe kupanda kuzichita munthu angathe kutaya chipulumutso.

Buku la Yakobo limaphunzitsa mwachimvekere kuti chikhulupiriro chopanda ntchito chili chakufa. Chikhulupiriro chochitachita kapena chikhulupiriro mwa Mulungu zimabweretsa ntchito zoyera ndi zopindulitsa. Pamene ntchito zabwino palibe zimasonyeza kuti pali chikondi chakufa komanso chikhulupiriro chopanda pake. Yesu anabwera kudzapulumutsa mtundu wa anthu ku

uchimo wonse kuti pakutero iwowo akhale anthu apaderapedera amene adzakhala achangu pochita ntchito zabwino (Tito 2:11-14).

Ndi kofunikira kubereka chipatso chabwino ndi kuonetsera ntchito zabwino ndi zachilungamo. Zimenezi sikuti zimapulumsa munthu ayi, komabe zimamuthandiza kuti akhazikike ndi kukula mu chidziwitso chake cha Mulungu.

NANGA MIPINGO IYO IMENE IMADZILENGEZA KUTI NDI YOKHAYO IMENE ILI NJIRA YOPITA KU CHIPULUMUTSO?

Yesu anati, "Ine ndine khomo; ngati wina alowa ndi Ine, adzapulumutsidwa" (Yohane 10:9). Palibe munthu, mpingo, kapena gulu la azibusa limene lingathe kupereka chipulumutso. Palibe chilichonse chimene tingachite kuti tiyenezedwe kapena tichigwiririre ntchito chipulumutso chathu.

Chipulumutso ndiyo mphatso ya Mulungu kudzera mwa Mwana wake ndipo palibenso njira ina.

Chimakhala ngati chitsanzo chenicheni cha kudzilungamitsa komanso kudzikuzi mu uzimu pamene mpingo unena kuti iwowo ndiwo khomo lolowera Kumwamba. Mpingo wa Mulungu wapangidwa ndi anthu amene aitanidwa ndipo apulumutsidwa ku uchimo. Uthenga wa mpingo

ndiwo wakulozera ena ku mtanda wa Khristu komanso ku chikhulupiriro cha Mau a Mulungu. Mbusa aliyense kapena gulu la anthu limene liphunzitsa zakuti timapulumsidwa mwa ntchito zathu kapena kuphunzitsa kuti munthu ayenera kudzera mwa iwowo ngati akufuna kukumana ndi Mulungu akupotoza uthenga woona wa Khristu. Zimenezi zikusiyana chiphunzitsa chimene ifeyo tinaphunzira. Iwo amene amaphunzitsa zimenezi akulakwitsa ndipo tiyenera kuwapewa (Aroma 16:17).

—mws



KODI MUKUDZIWA?

Pakuti ife tonse takhala ngati wina amene ali wosakonzeka; ndi zolungama zathu zonse zili ngati chovala chodetsedwa. —Yesaya 64:6

Mulungu anawaona Aisraele ngati odetsedwa ndi onyansa ngakhale amapemphera, amapereka nsembe, amachita ntchito zachifundo komanso kuyamika. Iye anadana ndi machitidwe a chipembedzo chifukwa amasakaniza izi ndi chinyengo.

Chiyero chao chinali ngati chovala chodetsedwa. Moyo wao woonetsa ntchito zabwino kunja umatengedwa ngati chidetso chenicheni. Mau akuti "chovala chodetsedwa" pa chinenero cha chiHeberi akutanthauza "chovala chogwiritsidwa ntchito ndi mzimai pa nthawi yake yapamwezi."



Mau a pa
Nyengo Yake

Ulalikire Uthenga Umene Ndikuuza

KUTI MUTIPEZE

The Gospel Truth
605 Bishops Ct.
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

Nyamuka, pita ku Nineve mudzi waukulu uja, nuulalikire uthenga umene ndikuuza.

—Yona 3:2


Mulungu anamupatsa mneneri Yona utumiki wopita ku Nineve ndi kumuza kuti "ulalikire uthenga umene ndikuuza." Aneneri ena sangasangalatsidwe, anthu sangakondwere nazo, ndiponso simungayamikiridwe chifukwa cha nsembe yanu. Mwina akhoza kukuthamangitsani m'tauni imene mukukhala, komabe mukhale wokhulupirika.

Musalalikire maganizo anu kapena nzeru zanu, koma zimene Mzimu wakuuzani mulalikire mwachikondi, moweruza ndi mwa kulimbika mtima kwa Mzimu Woyera.

Si ntchito ya utumiki kuti cholinga chatu chikhale chopangitsa kuti nkhosha zimve kukoma. Ngakhale pali nthawi zina zimene pa utumiki timafunika kutonthoza ndi kulimbikitsa nkhosha, anthu nthawi zambiri amakula pamene akumana ndi zosautsa komanso zokhoma. Kodi utumiki ungakule bwanji ngati palibe kulalikira chimene Mzimu akunena?

Mdirekezi amayesetsa kumanga pakamwa pa aliyense amene ali mtumiki weniweni wa Mulungu. Ukalalikira chimenechi, munthu uyo akhumudwa nazo. Ukalalikiranso ichi, wina wake sasangalala nacho. Posakhalitsa, nthawi yovomerezeka yolalikira uthenga pa mitu ina siidzapezeka. Tikatero ndiye tichiteno chiyani? Kodi tigonjere ku mphamvu zitizo? Kodi tilalikira chiyani?

Lalikirani Uthenga. Lalikirani choonadi. Lalikirani zimene Mulungu wakuuzani kuti mulalikire pamene lye wakuyitanani kuti mutero. Musaope munthu. Musachite mantha ndi udindo wanu. Musaope anzanu. Nthawi zina mwina mudzakhala nokha, komabe Mulungu ndi wokhulupirika kwa amithenga ake ndi ku choonadi Chake.



CHIYERO CHA KWA AMBUYE

—mws